-Kodi chifukwa chiyani anthu safuna kumvera Mawu a Mulungu?
-Chifukwa chakuti amalikonda tchimo lawo.

-Kodi mukufuna kukhalabe mu mdima, kapena mukufuna kumvera ku Mawu a Mulungu?



PHUNZIRO LA 51

1. Kodi Yesu anayamba liti kuŵaphunzitsa Ayuda?
-Pamene Yohane M'batizi anayikidwa m'ndende, Yesu anayamba kuŵaphunzitsa Ayuda.

2. Yasu anayamba kuŵaphunzitsa Ayuda ali ndi zaka zingati?
-Ali ndi zaka 30.

3. Kodi Nkhani Zabwino za Mulungu zimene Yesu anaŵaphunzitsa anthu zinali zotani?
-Nkhani Zabwino za Mulungu zinali zakuti ngakhale kuti machimo onse a anthu ayenera kulandira chilango cha imfa yosatha, Mulungu ankatumiza Mpulumutsi kudzaŵapulumutsa anthu onsewo

4. Kodi Mpulumutsi amene anamutumiza Mulungu kudzaŵapulumutsa anthu anali ndani?
-Yesu.

5. Kodi Yesu ankatanthawuza kuti chiyani pamene analankhula kuti, "Ndaŵi yakwana ndipo Ufumu wa Mulungu wayandikira?"
-Yesu ankatanthawuza kuti nthaŵi yakwana yakuti Ufumu wa Mulungu ugonjetse ufumu wa Satana ndipo Mpulumutsi adzamugonjetsa Satana.

6. Kodi ndi njira yanji imene munthu angathe kumusangalatsa nayo Mulungu?
-Pokhulupilira M'mawu a Mulungu.

7. Kodi chifukwa chiyani Yesu anaŵayitana anthu ena kuti adzikhala ndi Iye?
-Chifukwa chakuti ankafuna kuti aŵaphunzitse iwowo ndi cholinga chakuti nawonso adzaŵaphunzitse anthu ena Mawu a Mulungu.

8. Kodi ntchito ya anthu ena amene anayitanidwa ndi Yesu kuti adzikhala naye inali yotani?
-Ena anali asodzi a a msomba.

9. Kodi aphunzitsi a malamulo anali ndani?
-Anali Afarisi.

10. Kodi chiphunzitso cha Yesu ndi Afarisi chinkasiyana bwanji?
-Chifukwa chakuti Yesu anali Mulungu, ankamudziŵa Mulungu Atate.
-Afarisi sankamudziŵa Mulungu Atate.
-Chifukwa chakuti Yesu anali Mulungu, Iye ankaŵadziŵa bwino Mawu a Mulungu
-Afarisi sankaŵadziŵa bwino Mawu a Mulungu.
-Chifukwa chakuti Yesu anali Mulungu, Yesu ankakhulupilira mu liwu lililonse la Mulungu.
-Afarisi sankaŵakhulupilira Mawu a Mulungu.

11. Pachiyambi, kodi ziwanda zinali chiyani zisanakhale ziwanda?
-Pachiyambi, ziwanda zinali angelo abwino amene analengedwa ndi Mulungu mpaka pamene anamutsata Satana ndikusanduka kukhala oyipa.

12. Kodi chiwandacho chinadziŵa kuti amene ankaphunzitsayo anali Yesu?
-Inde.

13. Kodi chifukwa chiyani chiwandacho chinkamuwopa Yesu?
-Chifukwa chakuti chinkadziŵa kuti Yesu anali ndi mphamvu yochitumiza ichocho ku Nyanja ya Moto Wosatha nthaŵi iliyonse.

14. Kodi khate ndi tchimo zinkafanana bwanji?



18-[Yesu anati] “Aliyense okhulupilira mwa Iye, saweruzidwa, koma iye osakhulupilira waweruzidwa ngakhale tsopano, chifukwa chakuti sanakhulupilire mu dzina la Mwana wa Mulungu obadwa yekha.”

-Yesu analankhula kuti anthu amene akukhulupilira mwa Iye sadzaweruzidwa ndi Mulungu.

-Yesu analankhulanso kuti anthu amene sakukhulupilira mwa Iye, ali oyimbidwa kale milandu chifukwa chakuti sakukhulupilira kuti Yesu ndi Mpulumutsi.

-Kodi china chiyani chimene analankhula Yesu kwa Nikodemasi?

Tiyeni tiŵerenge Yohane 3:19-20

19-[Yesu anati] “Koma chiweruziro ndi ichi: Kuwunika kunadza pa dziko la pansi, koma anthu anakonda mdima koposa kuwunika chifukwa chakuti tchito zawo zinali zoyipa.
20-Pakuti aliyense ochita zoyipa,adana nako kuwunika, ndipo sakudza kwa kuwunika chifukwa chakuti zingawonekere ntchito zache.”

-Yesu analankhula kuti Iye ndi Kuwala amene wabwera m’dziko la pansi lino.

-Yesu analankhula kuti anthu osalungama safuna kuwala.
-Yesu analankhula kuti anthu osalungama amafuna kutsalirabe mu mdima.

-Kodi chifukwa chiyani anthu osalungama amafuna kutsalirabe mu mdima?
-Chifukwa chakuti amalikonda tchimo lawo.

-Mulungu anatumiza Yesu Mpulumutsi chifukwa chakuti Iye amaŵakonda anthu onse.

-Ngati tikukhulupilira mwa Yesu, sitidzafa koma tidzakhala ndi moyo osatha ndi Mulungu.

-Kodi china chiyani chimene analankhula Yesu kwa Nikodemasi?

Tiyeni tiŵerenge Yohane 3:17

17-[Yesu anati] "Pakuti Mulungu sanatumize Mwana wache pa dziko la pansi kuti akaweruze dziko la pansi, koma kuti dziko la pansi likapulumutsidwe ndi Iye."

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu anamutumiza Yesu pa dziko la pansi pano?

-Kodi Mulungu anamutumiza Yesu kudzaliweruza dziko la pansi?
-Iyayi.

-Kodi Mulungu anamutumiza Yesu kudzaŵawononga anthu?
-Iyayi.

-Mulungu anamutumiza Yesu kudzaŵapulumutsa anthu ku mphamvu ya tchimo.
-Mulungu anamutumiza Yesu kudzaŵapulumutsa anthu ku mphamvu ya imfa.
-Mulungu anamutumiza Yesu kudzaŵapulumutsa anthu ku mphamvu ya Satana.

-Kodi china chiyani chimene analankhula Yesu kwa Nikodemasi?

Tiyeni tiŵerenge Yohane 3:18



-Ngati m'mene sangathere anthu kudzichiza okha ku khate, chomchonso anthu onse sangathe kudzichiza okha ku tchimo.
-Ngati m'mene analili Yesu yekha poŵachiza anthu ku khate, chomchonso ndi Yesu yekha amene angathe kutichiza ife ku tchimo.

-Usiku wina munthu wina wache dzina lache Nikodemasi, anapita kukamuyendera Yesu.

Tiyeni tiŵerenge Yohane 3:1-2

1-Koma panali munthu wa Afarisi, dzina lache Nikodemasi, mkulu wa Ayuda.
2-Iye anadza kwa Yesu usiku, ndipo anati kwa Iye, "Rabi, ife tidziŵa kuti Inu ndinu mphunzitsi ochokera kwa Mulungu. Pakuti palibenso munthu amene akhoza kuchita zizindikiro zodabwitsa zimene Inu mukuchitazi, ngati Mulungu sali ndi iye."

-Afarisi ambiri ankamuda Yesu.
-Afarisi ambiri ankanena kuti mphamvu ya Yesu inkachokera kwa Satana.

-Nikodemasi anali osiyana ndi Afarisi enawo.
-Nikodemasi sankamuda Yesu.

-Nikodemasi ankafuna kuti alankhulane ndi Yesu ndipo amufunse Iye mafunso ambiri.

-Kodi Nikodemasi ananena chiyani kwa Yesu?
-Nikodemasi ananena kuti ankadziŵa kuti Mulungu ndi amene anamutumiza Yesu.

-Kodi Nikodemasi anadziŵa bwanji kuti Mulungu ndi amene anamutumiza Yesu?
-Chifukwa chakuti Yesu ankachita zozizwitsa zambiri

zimene zingachitidwe ndi Mulungu yekha.

-Kodi Yesu anayankha chiyani kwa Nikodemasi?

Tiyeni tiŵerenge Yohane 3:3

3-Yesu anayankha nati kwa iye, “Ndikukuwuza zowona, palibe amene angawuwone Ufumu wa Mulungu ngati sabadwanso kachiŵiri.”

-Yesu ananena kuti palibe amene angawuwone ufumu wa kumwamba asanabadwenso kachiŵiri.

-Kodi Yesu ankatanthawuza chiyani?
-Yesu ankatanthawuza kuti anthu onse akubadwa ali pasi pa ufumu wa Satana, ndipo ayenera kubadwanso kachiŵiri.

-Kodi anthu onse anabadwa bwanji ali pansi pa ufumu wa Satana?
-Pamene Adamu ndi Hava anachimwa ndikusamumvera Mulungu, anasiyanitsidwa ndi ufumu wa Mulungu.

-Pamene Adamu ndi Hava anachimwa ndikusamumvera Mulungu, anakhala pansi pa ufumu wa Satana.

-Ana a Adamu ndi Hava, Kayini ndi Abele anabadwa ali pansi pa ufumu wa Satana.

-Chifukwa chakuti Adamu ndi Hava anamuchimwira ndikusamumvera Mulungu, anthu onse anabadwa ali pansi pa ufumu wa Satana.

-Yesu ankatanthawuza kuti anthu onse anabadwa ali pansi pa ufumu wa Satana, chomcho ayenera kubadwanso kachiŵiri.

-Kodi Nekodemasi anayankha chiyani?



-Kenako, Mulungu anamuwuza Mose kuti apange njoka ya mkuwa ndipo ayipachike pa mtengo.

-Mulungu anati kuti aŵachiritsa a Isirayeli amene ayang’ane pa njoka pa mkuwayo.

-Kodi a Isirayeli anakatha kudzipulumutsa okha ku imfayo?
-Iyayi.

-Kodi ndi ndani yekha amene anakatha kuŵapulumutsa a Isirayeli ku imfayo?
-Mulungu.

-Kodi Yesu akufanana bwanji ndi njoka ya mkuwa imene Mulungu anamulamula Mose kuti apange m’chipululu muja?

-Apa pali zimene analankhula Yesu:

-Yesu adzapachikidwa ngati m’mene njoka ya mkuwa inapachikidwira pa mtengo.

-Yesu adzaŵapulumutsa anthu amene akumukhulupilira Iye ngati m’mene anapulumutsidwira a Isirayeli amene anayang’ana pa njoka ya mkuwa ija.

-Kodi china chiyani chimene analankhula Yesu kwa Nikodemasi?

Tiyeni tiŵerenge Yohane 3:16

16-[Yesu anati] “Pakuti Mulungu analikonda dziko la pansi kotero kuti anapereka Mwana wache obadwa yekha, kuti aliyense okhulupilira mwa Iye asatayike, koma akhale ndi moyo osatha.”

-Osakhala anthu akuda ndi oyera, ayi.
-Osakhala olemera ndi osawuka, ayi.

-Kwa Mulungu, anthu a mitundu yiŵiri amene ali pa dziko la pansi pano ndi amene abadwa kamodzi ndi amene abadwanso kachiŵiri.

-Anthu oyamba ndi amene anabadwa kamodzi ndipo akadali pansi pa mphamvu ya Satana.

-Anthu achiŵiri ndi amene abadwanso kachiŵiri, ndipo ali opulumutsidwa ndi mphamvu ya Mulungu.

-Anthu amene abadwa kamodzi kokha ali m'banja la Satana.

-Anthu amene abadwanso kachiŵiri ali m'banja la Mulungu.

-Kodi china ndi chiyani chimene analankhula Yesu kwa Nikodemasi?

Tiyeni tiŵerenge Yohane 3:14-15

14-[Yesu anati] Mwana wa munthu ayenera kupachikidwa ngati m'mene anapachikira njoka ya mkuwa Mose m'chipululu,
15-kuti aliyense okhulupilira mwa Iye akhale nawo moyo osatha."

-Kodi mukuyikumbukira nkhani ya Mose ndi njoka ya mkuwa m'chipululu muja?

-Chifukwa chakuti a Isirayeli anachimwa ndi kusamumvera Mulungu, Mulungu anatumiza njoka za ululu kuti zikaŵalume iwowo.
-A Isirayeli ambiri atafa, iwo amene anapulumuka analapa machimo awo.



Tiyeni tiŵerenge Yohane 3:4

4-Nikodemasi anafunsa kuti, "Kodi munthu angathe bwanji kubadwanso kachiŵiri atakalamba?" Ndithu, sangathe kuloŵanso m'mimba mwa amache ndi kubadwanso kachiŵiri!"

-Nikodemasi sanamumvetsetse Yesu zimene ankatanthawuza.
-Nikodemasi sankadziŵa kuti munthu angabadwenso bwanji kachiŵiri.

-Nikodemasi ankaganiza kuti Yesu ankatanthawuza za kubadwanso kachiŵiri ka thupi lathu.

-Kodi Yesu ankatanthawuza za kubadwanso kachiŵiri ka thupi lathu?
-Iyayi.

-Kodi Yesu anayankha chiyani?

Tiyeni tiŵerenge Yohane 3:5

5-Yesu anayankha kuti, "Ndikukuwuza zowona, palibe amene angaloŵe mu Ufumu wa Mulungu pokhapokhapo atabadwanso ndi madzi ndi Mzimu."

-Yesu ananena kuti tiyenera kubadwanso kachiŵiri mwa madzi ndi Mzimu.
-Yesu ananena kuti poyamba tiyenera kubadwanso mwa madzi.
-Kodi kutanthawuza kwache ndi chiyani kunena kuti, "kubadwanso mwa madzi?"

-Kodi "kubadwanso mwa madzi" kukutanthawuza "kubatizidwa?"

-Iyayi.

-Kodi Yesu ankatanthawuza kuti tiyenera kubatizidwa kuti tibadwenso kaŵiri?
-Iyayi.

-Kodi kubatizidwa kungatipulumutse ife?
-Iyayi.

-Kodi nanga Yesu ankatanthawuza chiyani ndi "kubadwanso mwa madzi?"
-Kodi madzi amachita chiyani kwa litsiro?
-Amachotsa litsiro.

-Yesu ankatanthawuza kuti anthu onse ayeretsedwe ku tchimo ngati m'mene madzi amachotsera litsiro.

-Yesu ankatanthawuza kuti anthu onse ayenera kulapa machimo awo kuti Mulungu aŵayeretse iwo ku machimo awo.

-Kachiŵiri, Yesu ananena kuti tiyenera kubadwanso mwa Mzimu.

-Kodi ankatanthawuza chiyani kuti, "kubadwanso mwa Mzimu?"
-Adamu ndi Hava atamuchimwira ndikusamumvera Mulungu, mzimu wawo unafa kwa Mulungu.
-Adamu ndi Hava atamuchimwira ndikusamumvera Mulungu, mzimu wawo umene unkayenera kudziwa, kukonda ndi kumumvera Mulungu unafa kwa Mulungu.

-Chifukwa chakuti mzimu wathu ndi wakufa kwa Mulungu, Mulungu ayenera kupereka moyo watsopano kwa mzimu wathu.

-Yesu ankatanthawuza kuti Mulungu Mzimu Woyera



ayenera kupereka moyo watsopano kwa mzimu wathu.

-Kubadwanso mwa madzi kukutanthawuza kuti tiyenera kulapa machimo athu kuti Mulungu atiyeretse ku machimo athuwo.

-Kubadwanso mwa Mzimu kukutanthawuza kuti Mulungu Mzimu Woyera ayenera kupereka moyo watsopano kwa mzimu wathu.

-Yesu anamuwuza Nikodemasi kuti asadabwe zakuti ayenera kubadwanso kachiŵiri.

Tiyeni tiŵerenge Yohane 3:7

7-[Yesu anati] "Usadabwe ndi kulankhula kwanga", "Uyenera kubadwanso kachiŵiri."

-Kodi chifukwa chiyani Nikodemasi sanayenere kudabwa za kubadwanso kachiŵiri?

-Apa pali zimene ananena Yesu.

Tiyeni tiŵerenge Yohane 3:6

6-[Yesu anati] "Chobadwa m'thupi chikhala thupi, ndipo chobadwa mwa Mzimu chikhala Mzimu.

-Kodi Yesu ankatanthawuza chiyani atanena kuti, "Mnofu umabereka mnofu, koma Mzimu umabereka Mzimu?"

-Yesu ankatanthawuza kuti mnofu ungathe kubereka mnofu okha, ndipo Mulungu Mzimu Woyera ndi amene angathe kubereka mzimu wa munthu.

-Kwa Mulungu, pali anthu a mitundu yiŵiri yokha pa dziko la pansi.